Kodi Mulungu ndi Mzimu kapena kanthu kena komwe tingakaone?

==================================================================

10. Mulungu ndi Mzimu. Pamene tikunena kuti Mulungu ndi Mzimu tikutanthauza kuti Iye sangaoneke. Iye akhoza kukhala kulikonse pa nthaŵi imodzi. Chimenechi ndi chovuta kwa ife kuti tichimvetsetse. Ife tili m'matupi amene amakhoza kukhala malo amodzi pa nthaŵi imodzi. Koma tikakhala pamalo amodzi tikhoza kukhala tikuganiza kuti tili malo ena. Ifenso tili ndi magawo ena omwe sangaoneke. Anthu amaona manja anu ndi nkhope yanu. Koma iwo sangaone maganizo anu. Mulungu yekha akhoza. Iye akhoza kuona zonse zimene tichita ndi zonse zimene timaganiza.

Yohane 4:24:
    Mulungu ndiye Mzimu omlambira Iye ayenera kumlambira muuzimu ndi m'choonadi.

Kodi tiyenera kuchita chiyani kwa Mulungu muuzimu ndi m'choonadi?

==================================================================

11. Tiyenera kumpembedza Iye. Ife tikhoza kupembedza Mulungu m'njira yabwino kapena m'njira yoipa. Kupembedza muuzimu kumatanthauza kupembedza pansi pa mitima yathu. Ife sitingathe kupembedza pongogwedeza milomo kapena matupi athu. Timapembedza pomaganiza zomwe tili kuchita. Timapembedza polemekeza Mulungu m'mitima yathu. Ife tikhoza kuwelama mitu yathu, kapena kugwada, ndi kumanena mawu komabe tisakuganizira kanthu.

Kodi tikungonena mawu osaganizira, kapena tikupembedza Mulungu muuzimu ndi m'choonadi?

==================================================================

12. Ayi, sitikutero. Ife tikhoza kumapereka ndalama kumpingo ndi kukhala okwiya m'mitima yathu. Tikhoza kufuna kudzisungira tokha ndalamazo. Tikhoza kumaimba nyimbo zotamanda Mulungu m'malo mwakuti anthu azititamanda.

Kodi ndi chifukwa chiyani kutereku sikuli kupembedza koonadi?

______________________________________________________________________

______________________________________________________________________

==========================================================================

13. Kumeneku sikupembedza koona chifukwa nkosachokera muuzimu. Ndi kongochokera m'thupi. Ndipo sikupembedza koonadi. Mulungu ndiye Mzimu. Popeza munthunso ndi mzimu ndi thupi, iye akhoza kukhala ndi chiyanjano ndi Mulungu. Koma mzimu wa munthu unaonongedwa chifukwa cha tchimo.

Taphunzira kale zimene zimachitika kwa ife pakubadwanso kwa tsopano. Kodi ndi chiyani? ______________________________________________________

______________________________________________________________________

==========================================================================

14. Pakubadwanso mwatsopano Mzimu Woyera amatipatsa moyo wa uzimu. Sitingathe kupembedza Mulungu moona pokhapokha titabadwanso mwatsopano. Yesu anadziŵa kuti Afarisi anazolowera kutsata malamulo ambiri popembedza. Iye anadziŵa kuti sangafune kusintha. Iwo akanakhoza kunena kuti, "Zakale ndi zabwino." Koma pamene anthu akhala ndi moyo watsopano mwa Khristu iwo amafuna kupembedza m'njira yolungama. Ndime iyi imatiuza ife za mmene tingapembedzere.

Yohane 4:24:

> Mulungu ndiye Mzimu, ndipo omlambira Iye ayenera kumlambira muuzimu ndi m'choonadi.

Imeneyi ndi ndime yabwino yoyenera kuikumbukira. Tsopano tengani nthaŵi yoiloweza pamtima ndimeyi. Ngati munganene mosaonera, yankhani funso ili: kodi ife tiyenera kupembedza Mulungu motani? Yankhani polemba Yohane 4:24: ______________________________________________________

______________________________________________________________________

==========================================================================

15. Mulungu amafuna kupembedza koona. Iye amafuna kuti anthu azimule-

mekeza. Iye amafuna kuti anthu azimutamanda ndi kumupembedza. Iye amafuna amene angachitedi zimenezi moona m'mitima mwawo. Iwo ayenera kuchita zimenezi pofuna kukondweretsa Mulungu osati anthu. Kufuna kukhala munthu wotere muyenera kupembedza Mulungu muuzimu ndi m'choonadi.

Kodi ndime imene imanena chomwechi imapezeka kuti?

______________________________

==========================================

16. Imapezeka mu Yohane 4:24:

Kodi ndi gulu la Ayuda liti mu nthaŵi ya Yesu limene linali kusunga malamulo ambiri ndipo silinathe kupembedza Mulungu moonadi?

______________________

Kodi ife tiyenera kupembedza Mulungu motani? Yankhani polemba Yohane 4:24: ______________________________

______________________________

______________________________

==========================================

ṢABATA LACHISANU: KHRISTU ATHANDIZA ANTHU
TSIKU LACHISANU: YESU APHUNZITSA ZA TSIKU LOPUMULA

1. Dzulo tinaphunzira njira yopembedzera Mulungu bwino.

Kodi ndi gulu liti la anthu mu nthaŵi ya Yesu lomwe linali kusunga malamulo ambiri koma sanali kupembedza Mulungu moonadi?

________________

Kodi ife tiyenera kupembedza Mulungu motani? Yankhani mwakulemba Yohane 4:24:

__________________________________________________

________________________________________________________

________________________________________________________

==========================================================================

2. Afarisi sanali kupembedza Mulungu moonadi. Mulungu ndiye Mzimu, ndipo onse omupembedza Iye ayenera kumupembedza muuzimu ndi m'choonadi.

Yesu anali ndi phunziro lina lalikulu lophunzitsa Afarisi. Afarisi anali kusunga sabata monga tsiku lopumula. Panalibe wina aliyense amene anali kugwira ntchito. Afarisi anati wina aliyense sayenera kuchita ulendo waufupi. Iwo anati Yesu sayenera kumachiritsa pa tsiku la sabata Koma Iye anali kuchiritsa. Chimenechi ndi chimene tikhale tikuchiphunzira kuchokera mphunziro limeneli.

(1) Tsiku la sabata la Ayuda lopuma ndi kupembedza linali loweruka.

(2) Akhristu anasintha tsikuli chifukwa Yesu anauka kwa akufa pa tsiku la sabata.

(3) Poonjezera kupembedza Mulungu ndi kupumula tiyenera kuchita ntchito zabwino pa tsiku la Mulungu.

Tsopano tengani Buku Lopatulika ndi kuwerenga Luka 6:1.11. Kodi ndi tsiku lanji limene Yesu anachiritsa munthu wopuwala dzanja?

________________

==========================================================================

3. Yesu anachiritsa munthuyo pa tsiku la sabata kapena kuti loweruka. Kwa Afarisi kuchiritsa munthu inali ntchito. Afarisi anati wina aliye-

nse asagwire ntchito pa tsiku loweruka.

Kodi Ayuda anati munthu ayenera kuchita chiyani pa tsiku loweruka?

______________________________________________________________________

==================================================================

4. Iwo amati munthu ayenera kupumula. Ndipo ayenera kupembedza Mulungu. Mulungu anapereka lamulo limeneli kwa Aisraeli. Liu lakuti "sabata" limatanthauza kupumula. Buku Lopatulika limanena kuti Mulungu anapanga dziko lonse lapansi pa masiku asanu ndi limodzi. Koma patsiku la chisanu ndi chiŵiri Iye anapumula. Tsono tsiku lachisanu ndi chiŵiri ndilo lopumula ndi kupembedza Mulungu.

Eksodo 20:9-10:

> Masiku asanu ndi limodzi uzigwira, ndi kumariza ntchito zako zonse; koma tsiku lachisanu ndi chiŵiri ndilo sabata la Yehova Mulungu wako; usagwire ntchito iliyonse."

Kodi ndi gulu liti la anthu limene linamvera lamulo limeneli?

______________________________________________

==================================================================

5. Anali Aisraeli kapena kuti Ayuda. M'nthaŵi ya Yesu tsiku lachisanu ndi chiŵiri linali tsiku lopumula ndi kupembedza. Linali kutchedwa kuti la sabata. Ku Yerusalemu kunali kachisi wamkulu ndi womangidwa mokongola. Anali kutchedwa kuti kachisi, ndipo kumeneko ndi kumene Ayuda anali kupembedzako. Koma m'mizinda yaing'ono ndi m'midzi munali myumba zazing'ono. Zimenezi zinali kutchedwa masunagoge. Ayuda a m'mizinda ing'onoing'ono anali kupembedza m'masunagoge.

Kodi ndi tsiku liti la pa Mulungu limene Ayuda linali sabata lawo kapena tsiku lopuma ndi kupembedza?

________________________________________

==================================================================

6. Linali tsiku loweruka. Taona kale kuti Yesu anali kupita kukapembedza ku masunagoge pa Chiweru. Iye anaphunzitsa m'masunagoge a Chiyuda ambiri. Pa tsiku lachiweru m'sunagoge ku Kapernao Iye anatulutsa

chiwanda mwa munthu.

Kodi ife timapumula ndi kupembedzabe pa tsiku loweluka? ______

Kodi ndi pa tsiku liti limene timapumula ndi kupembedza? ______

==========================================================================

7. Timachita zimenezi pa sabata. Mwina inu muli kudabwa kuti ndi chifukwa chiyani Akhristu sasunganso tsiku loweruka. Chifukwa chachikulu ndi chakuti Yesu anauka kwa akufa pa sabata. Pamene Iye anauka kwa akufa chidaonetsa kuti Iye anagonjetsa Satana. Iye analipira chilango cha machimo athu. Linali tsiku lalikulu pamene Iye anatsiriza ntchitoyi. Chifukwa cha chimenechi Akhristu tsopano amasunga sabata monga tsiku lopumula ndi kupembedza. Nthaŵi zina iwo amalitcha sabata kuti, ndi "tsiku la Ambuye."

Kodi ndi tsiku liti pa mlungu limene linali sabata la Ayuda lopumula ndi kupembedza?

______

==========================================================================

8. Tsiku lawo linali loweruka. Koma tsopano timasunga sabata monga tsiku lopumula ndi lopembedza. Chifukwa chachikulu cha chimenechi ndi chakuti Yesu anauka pa sabata. Kusunga tsiku loweruka inali mbali imodzi ya lamulo la Mose. Linali limodzi mwa malamulo khumi. Limeneli ndi limodzi la malamulo khumi omwe sanabwerezedwa m'Chipangano Chatsopano. Ife sitiuzidwa kuti tizisunga tsiku la sabata, limene liri loweruka. Ife timasunga sabata mmalo mwakuti tsiku limeneli ndi tsiku lomwe Yesu anauka kwa akufa.

Kodi ndi gulu liti la anthu lomwe limasunga sabata monga tsiku lopumula ndi lopembedza?

______

==========================================================================

9. Akhristu ndiwo amene amachita zimenezi. Amasunga tsiku loyamba la sabata mmalo mwa tsiku lachisanu ndi chiŵiri.

Marko 16:9:
Ndipo pamene Iye adauka m'mamaŵa tsiku loyamba la sabata, anayamba kuonekera kwa Mariya wa Magadala, amene Iye anamtulutsa ziwanda zisanu ndi ziŵiri.

Ayuda anali ndi tsiku lawo lopumula ndi lopembedza pa chiweru. Kodi ndi tsiku liti pakati pa sabata limene Yesu anauka kwa akufa?

____________

==========================================================================

10. Iye anauka pa sabata. Akhristu ampingo woyamba anali kukomana pa tsiku loyamba la sabata.

Machitidwe 20:7:
Ndipo tsiku loyamba la sabata, posonkhana ife kunyema mkate, Paulo anaŵafotokozera mawu.

Kodi ndi chifukwa chiyani tsiku lopumula ndi lopembedza la Akhristu lidasinthika ndi kukhala la sabata?

____________________________

____________________________________________________________

==========================================================================

11. Linasinthika chifukwa Yesu anauka kwa akufa pa tsiku la sabata. Luka 6 amene tawerenga lero taona Yesu ali ndi ophunzira. Iwo anali kupita modutsa pakati m'munda wa tirigu la chiweru. Ophunzira anali kutola ngala ndi kuzipukuta ndi kuzidya. Afarisi sanakondwere ndi zimenezi. Iwo anafunsa ophunzira kuti ndi chifukwa chiyani iwo anali kuchita zimenezi.

Kodi mukuganiza kuti Afarisi sanafune kuti ophunzirawo azitola ngalazo pa chiweru?

________________________________________________

==========================================================================

12. Afarisi anali kunena kuti anthu ayenera kupumula pa sabata. Iwo anali kunena kuti akuphunzira anali kugwira ntchito. Mukukumbukira kuti Afarisi anali kutsata malamulo ambiri pamapembedzedwe awo. Iwo anaonjezera malamulo awo ena ambiri pa malamulo a Mulungu. Iwo anali kuonetsetsa Yesu kuti amuone ngati angaphwanye malamulo awo. Pamene Iye anachi-

ta zimenezi, iwo anali kulankhula zoipa za Iye. Iwo anali kuyesetsa kwambiri kuti apeze tchimo mwa Iye.

Kodi ndi chifukwa chiyani tsiku lopumula ndi lopembedza Akhristu linasinthidwa kukhala la sabata?

_______________________________________________

=========================================================================

13. Linasinthidwa chifukwa Yesu anauka kuchokera kwa akufa pa sabata. Pamene Afarisi anali kulankhula zoipa za Yesu, Iye anaŵakumbutsa za Davide. Pamene Davide anali ndi njala anapita kunyumba ya Mulungu. Iye anapempha mkate umene ansembe anayenera kuudya. Davide sanali kudya mkate wotere nthaŵi zonse. Koma panthaŵi ya kusoŵa kwambiri analoredwa kuti adye. Yesu ananena kuti Iye anali ndi mphamvu kuposa sabata.

Marko 2:27-28:

> Ndipo ananena nawo, "sabata linaikidwa chifukwa cha munthu, si munthu chifukwa cha sabata; kotero Mwana wa munthu ali mwini dzuŵa la sabata lomwe.

Monga taphunzira dzulo, kodi ndi anthu ati amene anayesa kusunga malamulo ambiri koma sanapembedze Mulungu moonadi?

_______________________________________________

=========================================================================

14. Iwo anali Afarisi. Iwo anali ndi malamulo ambiri koma sanali kutumikira Mulungu. Iwo sanasamalire za kuthandiza anthu ena. Iwo anali kunena kuti loweruka linali longopumula. Ndipo wina wake anadza amene anawaonetsa kuti anali kulakwa. Iye anaonetsa kuti kunali kwabwino kuchita zinthu zabwino pa tsiku lopumula ndi lopembedza.

Luka 6:9:

> Ndipo Yesu anati kwa iwo, "ndikufunsani inu, kodi nkulola tsiku la sabata, kuchita zabwino, kapena kuchita zoipa, kupulumutsa moyo kapena kuuononga?

Kodi ndani anaonetsa kuti ndi kwabwino kuchita zinthu zabwino pa tsiku lopumula?

_______________________________________________

=========================================================================

15. Yesu anaonetsa zimenezi. Yesu anasunga sabata monga tsiku lopumula ndi lopembedza. Koma Iye anati ndi kwabwino kupulumutsa moyo. Ife tiyenera kuchita ntchito yabwino ya chifundo yonga yochiritsa anthu pa tsiku la Mulungu. Yesu anafuna kuonetsa Afarisi kuti chimenechi ndi chabwino. Motero Iye anaitana munthu wonuwala dzanja. Munthuyo anafika naimirira pambali pake pa Yesu.

Luka 6:10:

Ndipo pamene anaunguzaunguza pa iwo onse, anati kwa iye, "Tansa dzanja lako." Ndipo iye anatero, ndi dzanja lake linabwerera momwe. Koma iwowo anagwidwa ndi misala (kapena mkwiyo).

Kodi Afarisi anaona kuti pazichitika chiyani pa tsiku la sabata mmalo mochita ntchito zabwino?

________________________________________

____________________________________________________________

==============================================================

16. Iwo anati anthu ayenera kupumula ndi kupembedza Mulungu.

Kuonjezera kupumula ndi kupembedza Mulungu, kodi Yesu anati chabwino ndi chiyani choyenera kuchita tsiku la Mulungu?

______________________________

________________________________________________________

==============================================================

17. Tiyenera kuchita ntchito zabwino. Tiyenera kuthandiza amene ali wosoŵa. Sabata liyenera kukhala kwa ife tsiku lopumula, lopembedza ndi lochita ntchito zabwino.

Kodi ndi tsiku liti la sabata la Ayuda lomwe linali lopumula ndi lopembedza?

____________________________

Kodi ndi chifukwa chiyani tsiku lopembedza ndi lopumula Akhristu lisasinthidwe kukhala sabata?

______________________________________

____________________________________________________________

18. Tsiku la Ayuda lopumula ndi lopembedza linali loweruka. Tsiku la Akhristu linasinthidwa chifukwa Yesu anauka kuchokera kwa akufa pa tsiku la sabata.

Kuchokera pa chiphunzitso cha Yesu, kuonjezera kupumula ndi kupembedza, kodi china ndi chiyani choyenera kuchita pa tsiku la Ambuye?

___

===

19. Tiyenera kuchita ntchito zabwino.

Lembani zinthu zinayi kapena kuti zisanu zimene muli kuganiza kuti Akhristu ayenera kuchita pa sabata. Musalembe mawu akuti, "ntchito zabwino" koma mungolemba ntchito zabwinozo.

___

___

===

20. Kodi ndi tsiku liti la mlungu limene linali sabata la Ayuda lopumula ndi kupembedza?

Kodi ndi chifukwa chiyani tsiku la Chikhristu lopumula ndi lopembedza linasinthidwa kukhala la sabata? ___

___

Kuchokera m'chiphunzitso cha Yesu, kuonjezera pa kupumula ndi kupembedza kodi china ndi chiyani chabwino choyenera kuchita pa tsiku la Mulungu?

___

___

===

SABATA LACHISANU NDI CHIMODZI: KHRISTU NDI OPHUNZIRA AKE
TSIKU LOYAMBA: IYE ANAITANA OPHUNZIRA KHUMI NDI AŴIRI APADERA

1. Sabata lapita tinaphunzira kanthu kena komwe Yesu anaphunzitsa za kupembedza.

Kodi ndi tsiku liti pa mlungu lomwe linali Sabata ya Ayuda lopuma ndi lopembedza?

______________________________

Kuchokera ku chiphunzitsa cha Yesu, poonjezera kupumula ndi kupembedza, kodi china ndi chiyani choyenera kuchita pa tsiku la Mulungu?

______________________________

==========================================================

2. Tsiku la Ayuda lopumula linali loweruka. Tsiku la Akhristu linasinthidwa kukhala la sabata chifukwa Yesu anauka pa tsiku limeneli. Kuonjezera kupumula ndi kupembedza pa Sande, timayenera kuchita ntchito zabwino. Zimenezi ndi zimene Yesu anaphunzitsa.

Afarisi anali kulankhula motsutsana ndi Yesu. Koma anthu anali kukonda kumva mawu ake. Iwo anali kumutsata Iye kuti azimva zimene ali kuphunzitsa. Iwo anali kufuna kukhala monga Iye ndi kumumvera. Kotero Yesu anali ndi ophunzira ambiri koma Iye anadzisankhira mwa iwo khumi ndi aŵiri kuti azichita ntchito yake. Lero tiphunzira ena mwa maina awo ndipo iwo anali:

| | |
|---|---|
| Petro | Mateyu |
| Andreya | Thomasi |
| Yakobo | Yakobo mwana wa Alifeyo |
| Yohane | Simoni |
| Filipo | Yudasi mwana wa Yakobo |
| Batalomeyo | Yudasi Isikaliyoti |

Tsopano tengani Buku Lopatulika ndi kuwerenga Luka 6:12 mpaka ndime ya 19. Werenganinso ndime imeneyi, kodi ndi ayani amene Yesu anaŵatcha atumwi?

______________________________

==========================================================

3. Iye anatcha khumi ndi aŵiriwo mwa ophunzira ake kukhala atumwi. Nthaŵi imeneyi Yesu anali ndi ophunzira ambiri. Koma Iye anadzisankhira ena kuti aphunzire kugwira ntchito yake. Iye anafuna kuŵaphunzitsa ndi kuwatuma kwina. "Atumwi amatanthauza kuti "otumidwa." Kotero Iye anaŵatcha iwo atumwi. Mmenemu ndi momwe Marko analembera.

Marko 3:14:

> Ndipo anaika khumi ndi aŵiri, kuti akhale ndi Iye,
> ndi kuti akaŵatumee kulalikira.

Kuchokera m'ndime imeneyi, kodi Yesu anafuna kuti ophunzira khumi ndi aŵiriwo azichita chiyani?

____________________________________________

===========================================================================

4. Iye anafuna kuti iwo azilalikira. Iye anafuna kuŵatumiza kwina. Ku Negeria mfumu imakhala ndi omutsatira ambiri. Ena amakhala naye. Iwo amamulemekeza ndi kumachita zonse zimene alikuŵauza kuti achite. Iwo amasamalira nyumba yake. Iwo amakonda kumusamalira. Ndipo iye amaŵatuma. Iye amaŵakhulupirira. Iye anaŵasankha pakati pa ena ambiri. Yesu analinso ndi omutsatira ambiri. Iye anali kusankha ena kuti azikhala naye. Iwo anali kupita naye kulikonse. Iwo anali kumumvera.

Kodi Yesu anasankha ophunzira apadera angati? __________________________

===========================================================================

5. Iye anasankha khumi ndi aŵiri. Ŵerengani maina awo.

| | |
|---|---|
| Petro | Mateyu |
| Andreya | Thomasi |
| Yakobo | Yakobo mwana Alifeyo |
| Yohane | Simoni |
| Filipo | Yudasi mwana wa Yakobo |
| Batalomeyo | Yudasi Isikaliyoti |

Ŵerenganinso mainaŵa. Aphimbeni ndipo yesani kunena asanu ndi limodzi. Ngati munganene asanu ndi limodzi osaonera yesani kuŵalemba osayang'anira.

(1) ________________________ (4)______________________________

(2) ________________________ (5)______________________________

(3) ______________________ (6) ______________________

====================================================================

6. Taphunzira kale zina za ena a mwa ophunzirawa. Mwina mukukumbukira ubale wa pakati pa Petro ndi Andreya. Iwo anali asodzi. Petro anali kutchedwanso kuti Simoni. Iye anali wokwatira. Iye anakhala mtsogoleri wa ophunzira khumi ndi aŵiriwo. Iye anakana Khristu koma analapa. Kupyolera mwa ulaliki wake mazana a anthu anapulumutsidwa.

Andreya anali mbale wake wa Petro. Iye anali wophunzira wa Yohane Mbatizi. Pamene iye anakumana ndi Yesu anapita nakauza Petro. Andreya anapeza mnyamata yemwe anali ndi msomba ndi mkate zimene zinagwiritsidwa ntchito yodyetsa anthu zikwi zisanu (5,000).

Kodi Petro ndi Andreya anakhala ophunzira ayani? ______________________

====================================================================

7. Iwo anakhala ophunzira a Yesu. Yesu anasankhanso anthu aŵiri apa chibale. Iwo anali Yakobo ndi Yohane ana aamuna a Zebedayo. Zebedayo anali msodzi wa nsomba, kotero Yakobo ndi Yohane anali asodzi a anthu. Iwo anali kutchedwa "ana a bingu" ndi Yesu. Yesu atabwerera kumwamba, Yakobo anaphedwa ndi Herode agripa.

Nthaŵi zina Yohane anali kutchedwa kuti wophunzira amene Yesu anamkonda. Pamene iye anali wokalamba; anapititsidwa ku chisumbu cha Patmo chifukwa cha ulaliki wake. Iye analemba uthenga wa Yohane, makalata atatu a Yohane, ndi chibvumbulutso.

Yakobo ndi Yohane anali abale. Kodi ndi abale oyamba ati amene Yesu anaŵaitana?

(1) ______________________ M(2) ______________________

====================================================================

8. Poyamba Petro ndi Andreya anali paubale. Kachiŵiri Yakobo ndi Yohane anali paubale. Yesu anaitananso Filipo ndi Batalomeyo kapena kuti Nataniyeli. Anthu ameneŵa sanali paubale ayi.

Yohane 1:43,45:

M'maŵa mwake anafuna (Yesu) kutuluka kunka ku Galileya, napeża Filipo. Ndipo Yesu ananena naye, "Tsata Ine." ... Filipo anapeza Nataniyeli, nanena naye, "Iye amene Mose

analembera za Iye m'chilamulo, ndi aneneri, tampeza ndiye Yesu wa ku Nazarete."

Tsiku lina Filipo anabweretsa a Greek kwa Yesu. Koma iyeyu si Filipo mkulu wampingo wa m'buku la Machitidwe uja ayi. Batalomeyo amatanthauza kuti "Mwana wa Tolimayi." Ophunzira ameneyu dzina lake lenileni anali Nataniyeli. Iye anabadwira ku Kana komwe Yesu anasandutsa madzi kukhala Vinyo.

Kodi ndi abale ati amene anali ana a amuna a Zebedayo, msodzi wa msomba?

(1) ______________________________

(2) ______________________________

==========================================================================

9. Ana a amuna a zebedayo anali Yakobo ndi Yohane. Ataitanidwa iwoŵa Filipo ndi Batolomeyo anaitanidwanso. Ophunzira ena aŵiri anali Mateyu ndi Thomasi. Dzina lakale la Mateyu linali Levi. Taona kale mmene Yesu anamuitanira kuchokera mu ofesi ya msonkho. Iye anamupangira Yesu phwando patapita nthaŵi iye analemba buku la Mateyu.

Thomasi amatanthauza "Mapasa." Thomasi anali wolimba mtima. Nthaŵi ina pamene anaganiza kuti Yesu akhoza kukaphedwa iye anati, "Tiyeni tipite naye, kuti tikafe naye." Koma timakumbukira Thomasi chifukwa cha kukaika kwake. Iye anakaika kuti Yesu anauka kwa akufa kufukira iye anaona mabala a misomali m'manja mwake.

Kodi ndi ophunzira uti amene anabweretsa Batolomeyo (kapena kuti Nataniyeli kwa Yesu?

______________________________

==========================================================================

10. Anali Filipo amene amabweretsa Batolomeyo kwa Yesu. Koma Yesu anapeza Mateyu ndi Thomasi. Iwo anali ophunzira ena aŵiri amene anali ndi maina ofanana monga Simoni Petro ndi Yakobo. Iwo anali kutchedwa kuti Simoni Zeloti ndi Yakobo mwana wa Alifeyo. Simoni poyamba anali wankhondo. Iye asanatsate Yesu anali kumenyana ndi oŵeruza a m'dziko lake.

Yakobo wachiŵiriyo anali kutchedwa Yakobo wamnng'ono, kapena kuti Yakobo wochepa. Kutereku kunali kumusiyanitsa ndi Yakobo mbale wa Yohane. Yakobo wachiŵiriyo anali mwana wa Alifeyo.

Kodi ndi ophunzira uti amene anakaika kuti Yesu wauka kwa akufa?

______________________________________________________

==========================================================

11. Thomasi ndi amene anakaika. Panali ophunzira aŵiri amene anali kutchedwa Yidasi. Mmodzi anali Yudasi mwana wa Yakobo. Iye anali kutchedwa Taddeyasi.

Yudasi wina ndi amene anapereka Yesu. Yudasi Isikaliyoti anali mbala. Iye anali kusunga ndalama za Yesu ndi ophunzira ena. Koma iye nthaŵi zina anali kudzitengera ndalama kwa iye yekha. Iye anapereka Yesu chifukwa cha ndalama makumi atatu za siliva. Potsiriza pake anadzipachika yekha.

Kodi Yudasi Isikariyoti anasiya kugwira ntchito ya Khristu pa dziko lapansi?

____________________________

==========================================================

12. Yudasi Isikariyoti sanaleke kugwirira ntchito Khristu. Koma ophunzira ena khumi ndi mmodziyo anali kuchita zimene Yesu anali kunena. Iwo anali kuphunzira kuchokera kwa Iye. Iwo anali kuchita ntchito yake. Pamene Yesu anabwerera kumwamba, iwo anali kulalikira kulikonse.

Lembani maina asanu ndi limodzi a mwa ophunzira khumi ndi aŵiri omwe Yesu anaŵatcha atumwi.

(1) ____________________ (4) ____________________

(2) ____________________ (5) ____________________

(3) ____________________ (6) ____________________

==========================================================

13. Khumi ndi aŵiriwo anali Petro, Andreya, Yakobo, Filipo, Batolomeyo, Mateyu, Thomasi, Simoni, Yakobo mwana wa Alifeyo, Yudasi mwana wa Yakobo ndi Yudasi Isikariyote. Anthu khumi ndi aŵiriŵa anali kukhala ndi Yesu. Iwo anali ndi Iye kulikonse. Iwo anali kumvera chiphunzitso ndi ulaliki wake. Iwo anali kumuona ali kupanga zozizwitsa. Iwo anali kulankhula naye ndi kumufunsa mafunso. Yesu anali kuyankha mafunso awo. Iye anaŵaphunzitsa kupempheredwe. Iye anali kuwadzudzula akachita zolakwa.

Iye anali kuŵayamikira pamene iwo anali kuchita bwino.

Kodi timaŵatcha ayani anthu amene anakonda mphunzitsi wawo ndi kumumvera?

______________________________________________

===========================================================

14. Ophunzira khumi ndi aŵiri anakhala pafupi ndi Yesu. Iwo anali kuphunzira kuchokera kwa Iye tsiku ndi tsiku. Iwo anali kubweretsa mavuto awo kwa Iye. Kodi bwanji ife? Ifenso timayenera kukhala chifupi ndi Yesu. Ife timayenera kuphunzira pamene iye ali kulankhula kwa ife.

Mwina muli kunena kuti, "Kodi Yesu akhoza kulankhula bwanji kwa ine?" Iye amalankhula kwa inu kupyolera m'Buku Lopatulika. Iye amalankhulanso m'mitima yanu. Iye amalankhula kwa inu kupyolera mwa Akhristu ena. Iye amalankhula pokupangani kukhala okondwa pamene inu mumumvera ndi kukhala okwiya komanso pamene simutero. Inunso mukhoza kubweretsa mavuto anu kwa Iye mwa mapemphero. Inunso mukhoza kukhala ophunzira ake.

Lembani maina asanu ndi limodzi a mwa ophunzira khumi ndi aŵiri omwe Yesu anaŵatcha atumwi.

(1) ____________ (4) ____________

(2) ____________ (5) ____________

(3) ____________ (6) ____________

===========================================================

15. Khumi ndi aŵiriwo anali Petro, Andreya, Yakobo, Yohane, Filipo, Batolomeyo, Mateyu, Thomasi, Simoni, Yakobo mwana wa Alifeyo, Yudasi mwana wa Yakobo, ndi Yudasi Isikariyote. Ophunzira ameneŵa anakhala ndi Yesu. Iye anaŵaphunzitsa zinthu zambiri zimene sanaphunzitse ena. Iye anadziŵa kuti iwo azidzachita ntchito yake. Yesu anafera tchimo la munthu. Ndipo Iye anayenera kubwerera kwambmba. Ena adayenera kupititiza ntchito yake pansi pano.

Kodi mumafuna kukhala ophunzira wa Yesu wokhulupirika? ____________

===========================================================

16. Tidzakambirana za izi tonse pamodzi.

Lembani maina asanu ndi limodzi la mwa ophunzira khumi ndi mmodzi amene Yesu anaŵatcha atumwi.

(1) ______________________ (4) ______________________

(2) ______________________ (5) ______________________

(3) ______________________ (6) ______________________

SABATA LACHISANU NDI CHIMODZI: KHRISTU NDI OPHUNZIRA AKE
TSIKU LACHIŴIRI: OPHUNZIRA WOONA AMAKONDA NDI KUMVERA YESU

1. Taona kale kuti anthu ambiri anali kutsata Yesu. Koma Yesu anasankha khumi ndi aŵiri apadẹra ophunzira. Iye anafuna kuti aŵatumize kuchita ntchito yake.

Lembani maina asanu ndi limodzi la mwa ophunzira khumi ndi mmodzi amene Yesu anatcha atumwi.

(1) ____________ (4) ____________

(2) ____________ (4) ____________

(3) ____________ (6) ____________

==========================================================================

2. Akuphunzira khumi ndi aŵiriwo anali: Petro, Andreya, Yakobo, Yohane Filipo, Batolomeyo, Mateyu, Thomasi, Simoni, Yakobo, mwana wa Alifeyo. Yudasi mwana wa Yakobo ndi Yudasi Isikariyoti. Komatu siokhaŵa amene Yesu anafuna kuti amutsatire. Iye amafuna aliyense kukhala ophunzira wake.

Yesu anadziŵa kuti ambiri a mwa omutsatira ake sanali akuphunzira oonadi. Iwo anangofuna kuona zozizwitsa. Lero tiphunzira mmene ife monga ophunzira oonadi tingamachitire potsata Yesu.

(1) Tidzamukonda Iye
(2) Tidzamumvera Iye.

Tsopano tengani Buku Lopatulika ndi kuŵerenga Luka 9:23 mpaka 26. Tsopano werengani ndime ya 57 kufikira 62 pa mutu womwewo. Kodi aliyense amene Yesu anamuitana anakhala ophunzira?

____________

==========================================================================

3. Si aliyense anakhala ophunzira. Yesu anasankha ophunzira ake mosamalitsa. Iye anati, "Tsatani ine." Iye kaŵirikaŵiri anali kufotokoza kuti kukhala ophunzira okhulupirika kunali kutanthauza chiyani?

Luka 14:25-26:

Ndipo mipingo yambiri ya anthu anamuka naye; ndipo Iye anapotoloka nati kwa iwo; "Munthu akadza kwa Ine, wosada atate

wake ndi amake, ndi mkazi wake, ndi ana, ndi abale, ndi alongo ake, inde, ndi moyo wake womwe wa iye mwini sakhoza kukhala wophunzira wanga."

Kuchokera pa ndime imeneyi, kodi Yesu anati tizichita chiyani kwa mabanja athu mmalo mofuna kukhala ophunzira ake?

4. Yesu anati tiyenera kudana nawo. Yesu anagwiritsa ntchito mawu a mphamvu pamenepa. Koma iye sanatanthauze kuti tikhoze kuŵachitira zoipa ayi. Iye anatanthauza kuti ife tiyenera kumukonda Iye koposa wina aliyense. Timayenera kumukonda koposa makolo athu. Timayenera kumukonda iye koposa akazi ndi ana athu. Timayenera kumukonda Iye koposa ife eni. Nthaŵi zina timayenera kusankha pakati pa zimene Mulungu afuna ndi zimene ife tifuna. Timayenera kusankha njira ya Mulungu. Mmenemu ndi mmene timaonetsera chikondi chathu.

Ngati ife tili kufuna kukhala ophunzira oonadi, kodi Yesu anati tiyenera kukonda koposa ndani?

5. Timayenera kukonda Yesu. Kodi kukonda wina wake kumatanthauza chiyani? Ngati mkazi amakonda mwamuna wake adzamulemekeza. Iye adzafuna kutenga nthaŵi ndi iye. Iye adzamumvera ndipo adzayesetsa kumukondweretsa. Yesu amafuna omwe adzamukonda ndi kumumvera.

Ngati ife titamakonda ndi kumvera Yesu, kodi tidzakhala chiyani kwa Iye?

6. Tidzakhala ophunzira ake. Taona kuchokera pa Luka zimene Yesu ananena kwa ena a mwa ophunzira ake. Wina wake anafuna kudikira kuti atate ake ayambe afa kuti adzatsate Yesu bwino. Yesu anati amene alibe moyo wauzimu ayenera kuika mmanda akufa. Padakakhala anthu ena osamalira atate ake. Mateyu analemba motere.

Mateyu 8:21,22:

Ndipo wina wa ophunzira ake anati kwa Iye, "Ambuye, mundilole ine ndithange ndamuka kuika maliro a atate wanga." Koma Yesu ananena kwa iye, "Tsata Ine, nuleke akufa aike akufa awo."

Ngati ife tili ophunzira woonadi, kodi tidzachita chiyani ndi Yesu?

_______________________________________________

=================================================================

7. Ngati ife tili ophunzira woonadi tidzamukonda Iye. Mafumu athu a mu Afrika amakhala ndi oŵatsatira ambiri. Pobwezera ulemu mafumuwo amapereka zinthu zambiri kwa otsatirawo. Iwo amapereka ulemu, chitetezo ndi chuma. Koma Yesu anadziŵa kuti ophunzira ake adzavutika pomutsata Iye. Nthaŵi zina iwo adzadedwa. Nthaŵi zina iwo adzakhala opanda malo okhala. Nthaŵi zina iwo adzasiya mabanja awo. Yesu anafuna ophunzira amene adzamtsata chifukwa chomukonda Iye. Leronso ndi chimodzimodzi.

Luka 14:33:

Chifukwa chake tsono, yense wa inu amene sakaniza (kapena kusafuna kuzitaya) zonse ali nazo, sakhoza kukhala wophunzira wanga.

Kuchokera pa ndime imeneyi, kodi timayenera kuchita chiyani kuonetsa kuti timakonda Yesu koposa? _______________________________

_______________________________________________

=================================================================

8. Tiyenera kukhala ofunitsitsa kusiya zonse zimene tili nazo. Sitiyenera kukonda chilichonse kuposa Yesu. Komatu kutereku sikukwanira. Timayeneranso kumvera Yesu. Ngati timakonda Yesu, tidzamvera malamulo ake. Ngati ife sitiŵamvera, izi zimaonetsa kuti ife sitimukonda.

Yohane 14:21:

Iye wakukhala nawo malamulo anga, ndi kuŵasunga, iyeyu ndiye wondikonda Iñe.

Kodi njira yoyamba imene ife monga ophunzira tidzachita potsata Yesu ndi iti?

(1) _______________________________________

(2) Tidzamumvera Iye.